

UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso
kuchokera m'Baibulo kupita kwa
amene akulalikira Uthenga Wabwino

KUITANA KWAKUKULU ZEDI—AMBIRI AKUITANIDWA

(Fanizo limene Khristu ananena - Iolembedwa pa Mateyu 22:1-14)

Yesu ananena fanizo la phwando la ukwati wachifumu, kusonyeza kufunika kwa kuitana kwa Mulungu kwa anthu onse kuti apulumutsidwe.

Ufumu wa Mulungu uli ngati mfumu imene inakonzana phwando lalikulu la ukwati wa mwana wake. Mfumuyo inatuma antchito ake kuti akaitane anthu oitanidwa ku ukwatiwo, koma iwo sanafune kubwera. Mfumuyo inatumiza antchito ena nkuwauza tsatanetsatane wa chakudya chodabwitsa chimene chinakonzedwacho. Ndipo inati, “Bwerani ku ukwati, popeza zonse zakonzeka!”

Ambiri amene anaitanidwa anavomera koma mwachipongwe ndi kuonetsa kusalabadira, iwo anapitiriza zimene amachita, ena anapita kuminda yawo ndi ena kumisika yawo. Ndipo ena, pokwiya ndi mfumuyo, anazunza antchito ake aja ndipo pamapeto pake anawapha. Mfumuyo inamva za kusowa ulemu ndi kupanda chilungamo kwakukuluku ndipo inatumiza asilikali ake kukapha aupanduwo ndi kuononga mizinda yao.

Mfumuyo inauza antchito ake ena kuti: “Ukwati wakonzedwa, koma oitanidwawo sanafune kubwera. Ndipo antchitowo anapita, nachita monga inalamulira mfumu, naitana aliynse, wabwino ndi woipa omwe, kuti abwere kuphwando la ukwati. Posakhalitsa, ku ukwatiko kunadzaza ndi alendo.

Mfumuyo inabwera kudzaona oitanidwawo ndipo inaona munthu amene sanavale malaya a ukwati. Mfumuyo inafunsa kuti, “Mnzangawe, chifukwa chiyani unabwera wopanda chovala choyenera?” Munthuyo adangoti kukamwa

yasaa!. Mfumuyo inalamula antchito ake kuti am’ange munthuyo manja ndi miyendo ndi kumponya kunja kumdima, kumene kudzakhala kuzunzika kwakukululu.

Yesu anamaliza fanizoli ponena kuti: “Oitanidwa ndi ambiri, koma osankhidwa ndi owerengeka.”

Fanizoli limayala maziko a chiphunzitso chachikulu cha choonadi. Kuitana kwakukululu kumene kunaperekedwa ndiko kuitanira kwakuti tipulumutsidwe ku uchimo ndi kulandira madalitso a ufumu wa Mulungu. Kuitaniraku poyamba kunaperekedwa kwa Ayuda, koma iwo monga mtundu anakana Yesu Khristu ndipo anakana mwayi wakulapa ndi kusangalala ndi zinthu zabwino za Mulungu. Uthenga wabwino wachipulumutso kenaka unapekeredwa kwa Amitundu. Mulungu anapereka chipulumutso kwa anthu a m’banja lililonse, fuko lililonse, mtundu uliwonse ndi chinenero chilichonse. “Bwerani kuti mudzapulumutsidwe. Lapani ndi kulumikizidwa ndi Khristu, kuti mukalowe mu chimwemwe cha Ambuye.”

Anthu ambiri amakaikakaika, ndipo mwakachetechete amanyalanyaza kuitanidwa ku phwando la ukwati. Iwo ali otanganidwa ndi zosamalira za moyo ndipo alibe chidwi chotumikira Mulungu. Iwo amaika patsogolo ndalama, manyado, maphunziro, ntchito ndi zosangalatsa ndipo savomera kuitana kwa uthenga wabwino. Ena ndi otsutsa ndipo amapanduka ndi kulimbana ndi zinthu za Mulungu.

(Yapitirira pa tsamba 2)



“Kuitana kwakukululu kumene kunaperekedwa ndiko kuitanira kwakuti tipulumutsidwe ku uchimo ndi kulandira madalitso a ufumu wa Mulungu.”

ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;
Aef. 2:1, 5-6

Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

Chidzalo cha Mzimu Woyera

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

Chiyero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;
Akol. 1:18

Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

Chiyero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;
1 Akor. 7:10-11

Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;
Mat. 25:31-46

Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Ndikofunika kuzindikira kuti kuitanidwa kwa uthenga wabwino kwa anthu ONSE ndipo palibe amene akuchotsedwa. Mfumuyo inafuna kuti aliyense abwere ku mgonero wa ukwati, monga mmene Mulungu amafunira kuti anthu onse apulumuke masiku ano. Iye akukuitanani kuti mubwere kudzasangalala ndi mgonero wake wochuluka, m'moyo uno ndi m'moyo ulinkudzawo.

Mofanana ndi ukwati uliwonse, pamayenera kukhala zovala zoyenerera. M'nthawi ya Yesu, alendo anali kupatsidwa malaya a ukwati; iwo samadzipezera chovalacho. Mulungu wakonza kuti ONSE amene avomera kuitana kwake, aliyense wa iwo alandire mwinjiro wa chilungamo. Chilungamo chathu sichovala choyenera. Chovala chovomerezeka ndicho chipulumutso chimene Mulungu yekha angapereke. Komabe, kuti tilandire chipulumutso chimenechi, munthu aliyense payekha ayenera kuvomera kuitana kwa anthu onse kuti apulumutsidwe.



“Chilungamo
chathu sichovala
choyenera. Chovala
chovomerezeka
ndicho chipulumutso
chimene Mulungu
yekha angapereke.”

Sikokwanira kubwera ku tchalitchi kapena kusonkhana ndi ena. Tiyenera kuvekedwa chipulumutso. Ichi ndi chifukwa chake munthu wa mfanizo lija anasowa chonena, pakuti panalibe chowiringula. Anapatsidwa chovala koma anakana kuchivala. Kukana kwake kunabwera pamtengo woopsa: kulekanitsidwa kosatha ndi mfumu ndi kukakhala m'malo amazunzo.

Mulungu samakakamiza aliyense kulandira Yesu Khristu monga Mpulumutsi wao; komabe, ONSE ali

kuitanidwa. Ena amanyalanyaza kuitanako, ndipo ena amachedwa kuyankha. Ena amavomera koma amatsatabe ziphunzitso ndi njira zao ndipo amakana kuvomereza njira ya Mulungu ya chiyero. Monga mufanizoli, anthu onse amaitanidwa, koma si onse amene amasankhidwa kuti asangalale ndi madalitso a Mulungu chifukwa chakuti sakufuna kukwaniritsa zofunika.

Iwo amene asankhidwa ndi Mulungu nadalitsidwa m'moyo uno ndi wamuyaya, ndiwo amene avomera kuitanako ndi kuvala malaya a ukwati operekedwawo. Kuitana kwakukulu kwaperekedwa kwa ife tonse, koma tiyenera kusankha kuyankha ndi kuvala zovala za chipulumutso. Pakuti monga Yesu ananenera, “Oitanidwa ali ambiri, koma osankhidwa ali owerengeka.” Mulungu samana munthu aliyense mpata wakuti apulumuke. Mphatso ya Mulungu imaperekedwa kwaulere kwa onse mwa chisomo chake, koma munthu aliyense ayenera kusankha kuilandira.

Mnzanga, kodi wavomera kuitanaku? Kodi udzaima pa tsiku lalikululo utavekedwa chilungamo cha Khristu? Usachedwe, chifukwa chipulumutso chikuyembekezera. ■

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvumere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

Mau a Mkonzi



Ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe. — Yohane 7:37

Yesu akuitana aliyense kuti abwere makamaka amene ali ndi ludzu lamkati, iwo amene amalakalaka chinachake chakuya, chabwino, ndi chamuyaya. Ine ndine woyamikira kwambiri kuti taitanidwa kuti tipulumutsidwe. Chisomo cha Mulungu chimaperekedwa kwa onse, ndipo Iye amafuna kuti aliyense avomere mwachikhulupiriro.

Mutu wathu ulendo uno ndiwo “Kusankhidwa ndiponso ufulu wosankha.” Mafunso okhudza ziphunzitso pa nkhanzi akhala akukambidwa kwa zaka mazana ambiri. Chiphunzitso cha Calvinism chimene chazikika mu ziphunzitso monga — kusankha kopanda malire, chitetezero chokhala ndi malire, chisomo chosakanizidwa, ndi kupirira kwa oyera mtima—zimapotoza uthenga wabwino wa chipulumutso. Ziphunzitso zimenezi zimapaputsa choonadi cha m’Baibulo chakuti Mulungu amafuna kuti anthu onse apulumuke ku uchimo.

M’malo motsutsa cholakwika chilichonse, kalatayu akutsindika pa choonadicho — choperekedwa momveka bwino kudzera m’Malemba, —chakuti chipulumutso chimaperekedwa kwa onse ndipo chiyenera kulandiridwa kwaulere. Njira yabwino yothanirana ndi chiphunzitso chonyenga ndiyo choonadi. Tikamaphunzira Mau a Mulungu ndi kuwagawa moyenera, timakhala okonzeka kuzindikira ndi kukana zolakwika. Mavesi apaokha angaonekere kukhala ochirikiza ziphunzitso zina, koma tiyenera kuwamasulira Malemba mogwirizana ndi nkhanzi yake ndi molumikizana ndi nkhanzi yonse ya mu uthenga wabwino. Maziko a chiphunzitso cha Chipangano Chatsopano ndi akuti chipulumutso chimaperekedwa kwa onse—osati owerengeka okha okonzedweratu. Mulungu wapatsa munthu aliyense ufulu wosankha kulandira kapena kusalandira chisomo chake.

Malemba ambiri amene amatchula za *chisankho* amafotokoza za kuchoka pa pangano la Mulungu ndi Israele kupita ku kuitana kwa mpingo wa Chipangano Chatsopano. Tikamawerenga mau mu ndondomeko yake, zikuonekeratu kuti ndimezi sizikunena za chipulumutso cha munthu aliyense, koma za dongosolo lalikulu la chiombolo kudzera mwa Khristu.

Ukhoza kukhala uthenga wosakoma ndi wosulutsidwa ngati tinganene kuti Khristu sanafere onse komanso kuti mwazi wake umagwira ntchito kwa gulu lokhalo losankhidwiratu. Yamikani Mulungu, chifukwa chisomo chake chafikira kwa inu ndi kwa ine! M’chikondi chake chopambana, watipatsa ufulu wolandira kapena kukana mpatso ya chipulumutso.

Ngakhale kuti mutuwu sungakwanitse kufotokoza zonse mu phunziro limodzi, tikukhulupirira kuti maziko omveka akhazikitsidwa. Mzimu wa Mulungu ukutsogolereni kukumvetsetsa kozama ndikukhazikitsani inu molimba mu choonadi cha Mau ake.

Michael W. Smith

July 2025

NGATI MULUNGU AMADZIWA KALE CHILICHONSE,

KODI ZIKUTANTHAUZA KUTI TILIBE MWAI WOSANKHA?

Ayi. Ngakhale kuti Mulungu ndi wodziwa zonse ndiponso amalamulira pa zonse, Iye anatilenganso ndi mphamvu yakutha kusankha. Ngakhale Iye amadziwiratu zonse kotheratu sizimatanthauza kuti Iye ndiye amatsogolera zosankha zathu. Pamene zochitika za m’tsogolo zinaloseredwa pokhazikika pa chidziwitso cha Mulungu—chidziwitso chake changwiro cha zochitika zonse za m’tsogolo—zinalibe woziyambitsa, koma zinawululidwa.

Maulosi a m’Malemba, monga a m’buku la Daniele ndi Chivumbulutso, anavumbulidwa kuti asatsutsane ndi chifuniro cha munthu koma kuti asonyeze kuti Mulungu amadziwa mapeto kuyambira pachiyambi. **Kudziwiratu kwa Mulungu kumakulitsa ulamuliro wake popanda kuchepetsa ufulu wakudzisankhira wa munthu.**



Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

www.thegospeltruth.org

kuti mudzilandira makalata

athu kapenanso kuti

muone makalata akale.

**Zogwirizana ndi
Uthenga Wabwino
Wooni:
Kalata no. 28:
Chitetezo Chamuyaya**





Kalozera pophonzira Baibulo

Chisankho ndiponso ufulu wosankha

Ulamuliro, Chisomo, Kusankha, ndi Chipulumutso

Kuwerenga Malemba: Ndichititsa mboni lero, kumwamba ndi dziko lapansi zitsutse inu; ndaika pamaso panu moyo ndi imfa, mdalitso ndi temberero; potero, sankhani moyo, kuti mukhale ndi moyo, inu ndi mbeu zanu.
— Deuteronomo 30:19

Matanthauzo: Kusankha: Mchitidwe wa kusankha kapena kusankha kwa Mulungu. Zimamangirizidwa ku chisomo cha Mulungu ndi kudziwiratu, osati kukondera kapena kukakamiza.

Ufulu wosankha: Mphamvu zimene Mulungu anapatsa anthu posankha zochita. M'nkhani ya chipulumutso, zikunena za kuthekera kwa kuyankha kuitana kwa Mulungu—mwina mwa kuvomereza kapena kukana kupereka kwake kwa chisomo.

Mwachidule: Chisomo chachikulu cha Mulungu chimagwira ntchito limodzi ndi udindo wa munthu komanso ufulu wosankha. Mulungu anakonzeratu dongosolo lake la chipulumutso kudzera mu imfa ya Yesu Khristu, ndondomeko yofikira anthu onse. Amaitana, kutipempha kuti tiyankhe.

I. Mulungu alamulira pa zonse

- A. Yesaya 46:9-10 Uphungu wa Mulungu udzakhazikika.
- B. Daniele 4:35 Mulungu amachita monga mwa chifuniro chake.
- C. Kuitana kwa chipulumutso kwa onse.
- D. Yohane 3:16-17 Mulungu anakonda dziko lapansi.
- E. 1 Timoteo 2:4 Mulungu akufuna kuti onse apulumuke.
- F. 2 Petro 3:9 Sakufuna kuti ena awonongeke.
- G. Mateyu 11:28 Idzani kwa Ine.
- H. Chivumbulutso 22:17 Aliyense amene akufuna abwere.

- C. Ahebri 3:15 Musaumitse mitima yanu.
- D. Aroma 6:16 Inu mumasankha amene mungamumvere.
- E. 2 Petro 1:10 Tsimikizani maitanidwe ndi masankhidwe anu.

V. Kulandira kapena kukana chisomo

- A. Chivumbulutso 3:20 Ngati munthu aliyense amva ndi kutsegula.
- B. 2 Akorinto 6:1 Musalandire chisomo pachabe.
- C. Mateyu 23:37 Ndikufuna... inu simukufuna.
- D. Machitidwe 7:51 Inu mumakaniza Mzimu Woyera.
- E. Ahebri 5:9 Chipulumutso kwa iwo akumvera.
- F. Mac 24:25 Felikisi ananjenjemera koma anachedwa.

II. Khristu anafera onse

- A. 1 Timoteo 2:6 Anadzipereka yekha dipo la onse.
- B. 1 Yohane 2:2 Chikhululukiyo cha dziko lonse lapansi.
- C. Ahebri 2:9 Analawa imfa chifukwa cha munthu aliyense.
- D. 2 Akorinto 5:15 Iye anafera onse.
- E. Yohane 1:29 Mwanawankhosa achotsa uchimo wa dziko lapansi.

VI. Kusankhidwa kwa chisomo ndi kusankhidwiratu

- A. 2 Timoteo 1:9 Chipulumutso chinali ndi cholinga dziko lisanayambe.
- B. Aefeso 1:4-7 Osankhidwa dziko lisanakhazikike.
- C. Aefeso 1:10-11 Anakonzedweratu monga mwa cholinga chake.
- D. Aroma 8:28-30 Zodziwidwiratu, zokonzedweratu, zoitanidwa, zolungamitsidwa.
- E. Machitidwe 4:12 Chipulumutso sichikhala mwa wina aliyense.
- F. 2 Atesalonika 2:13 Osankhidwa kuyambira pachiyambi.
- G. 1 Petro 1:2 Osankhidwa mwachidziwitso cha Mulungu.
- H. Yohane 1:11-13 Osati mwa kufuna kwa munthu.
- I. Aroma 11:5-7 Otsalira mwa kusankha kwa chisomo.

III. Chipulumutso cha chisomo kudzera mu chikhulupiriro

- A. Aefeso 2:8-9 Opulumutsidwa ndi chisomo, osati ntchito.
- B. Tito 2:11-12 Chisomo chaonekera kwa anthu onse.
- C. Aroma 3:24 Kulungamitsidwa kwaulere ndi chisomo chake.
- D. Machitidwe 15:11 Opulumutsidwa ndi chisomo cha Yesu.

IV. Ufulu wosankha ndi kudzisankhira mwini

- A. Deuteronomo 30:19 Sankhani moyo ndi kukhala ndi moyo.
- B. Yoswa 24:15 Sankhani amene mukufuna kumtumikira.

Kumaliza

*Ndipo Mzimu ndi mkwatibwi anena, Idzani.
Ndipo wakumva anene, Idzani. Ndipo wakumva ludzu adze;
iye wofuna, atenge madzi a moyo kwaulere.
—Chivumbulutso 22:17*

Kusankhidwa kwa Chisomo

ULAMULIRO WA MULUNGU NDI KUYANKHA KWA UFULU WOSANKHA



Mulungu akuitana anthu onse ku chipulumutso, koma si onse amene amavomereza. Kodi ulamuliro waumulungu ndi kusankha kwa anthu zimakhallira pamodzi? Kusankhidwa kwa chisomo kumawonetsa ulamuliro wa Mulungu—komabe kumaitana moyo uliwonse kuyankha kuitana kwake. Chisankho chikhalabe chathu.

Dongosolo loposa la Mulungu la chipulumutso

Mulungu amalamulira mopambana. Chifuniro chake, zolinga zake, ndi dongosolo lake sizingalephereke. Monga momwe mneneri Yesaya ananenera, “Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzachita chifuniro changa chonse” (Yesaya 46:10). Mulungu amatsogolera zinthu zonse mogwirizana ndi nzeru ndi cholinga chake. Monga momwe Daniele ananenera, “achita monga mwa chifuniro chake... palibe woletsa dzanja lake” (Daniele 4:35). Izi zikuphatikiza dongosolo la Mulungu la chipulumutso. Mulungu anafuna kuombola anthu dziko lapansi lisanakhazikitsidwe. Chipulumutso sichinali mwachisawawa—chinali dongosolo ladlaladala la Mulungu, loikidwa kuwafikira anthu onse.

“Ngakhale kuti anthu angasankhe kuchita zinthu zosemphana ndi chifuniro cha Mulungu, ufulu umenewo ulipo chifukwa cha zimene Mulungu anakonza.”

Kuitanira padziko lonse kwa onse

Uthenga wabwino uli maitanidwe kwa anthu onse. Mulungu amakonda dziko lonse lapansi ndipo anapereka chipulumutso kwa “aliyense wokhulupirira Iye” (Yohane 3:16). Mulungu “afuna anthu onse apulumuke, nafike pozindikira choonadi.” (1 Timoteo 2:4) “Anthu onse adzapulumutsidwa, nafike pozindikira choonadi. Petro ananena chifuniro cha Mulungu kuti Ambuye “wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike kukulapa” (2 Petro 3:9). Kuitanira kwa Mzimu kumaperekedwa kwa onse: “Iye wofuna, amwe madzi a moyo kwaulere” (Chivumbulutso 22:17).

Yohane M’batizi analengeza kuti, “Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi” (Yohane 1:29). Kukhululukidwa sikusungidwa kwa osankhidwa ochepa. Yesu “anadzipeka yekha dipo la onse” (1 Timoteo 2:6) ndipo anakhala nsembe yotetezera “machimo a dziko lonse lapansi” (1 Yohane 2:2). Iye “anafera onse” (2 Akorinto 5:15) ndipo analawa “imfa m’malo mwa munthu aliyense” (Ahebri 2:9). Palibe amene akuchotsedwa!

Chipulumutso kudzera mu chisomo

Ngakhale kuti chimaperekedwa mwaufulu, chipulumutso sichimangochitika kapena kulandiridwa ndi aliyense. “Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo mwa

chikhulupiriro... osati mwa ntchito” (Aefeso 2:8-9). Chipulumutso sichimaperekedwa chifukwa cha udindo, ntchito, fuko, kapena kudziwika, koma mwa chisomo—kukonderedwa ndi Mulungu kosatiyenera. “Ayesedwa olungama kwaulere ndi chisomo chake kudzera mu chiombolo cha mwa Khristu Yesu” (Aroma 3:24). Chiombolo chimapezeka mwa “chisomo cha Ambuye Yesu Khristu” (Machitidwe 15:11). Ngakhale sichilandiridwa ndi onse, chisomo ichi chimaperekedwa kwa onse. “Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse” (Tito 2:11-12).

Mphamvu ya ufulu wosankha

Mulungu afuna kuti onse apulumuke, ndipo Khristu anafa kuti akwaniritse cholinga chaumulungu chimenechi. Komabe inalinso mbali ya dongosolo lalikulu la Mulungu linali kulenga anthu ndi ufulu wosankha. Chilengedwe cha Mulungu pa anthu kuti akhale ndi ufulu wodzisankhira chikugwirizana kwathunthu ndi ulamuliro wake. Ngakhale kuti anthu angasankhe kuchita zinthu zosemphana ndi chifuniro cha Mulungu, ufulu umenewo ulipo chifukwa cha zimene Mulungu anakonza.

Malemba amatsimikizira udindo wa munthu wosankha. “Ndaika pamaso panu moyo ndi imfa... potero sankhani moyo” (Deuteronomo 30:19). Chimodzimodzi, Yoswa anafunsa anthu kuti: “Sankhani lero amene mudzamtumikira” (Yoswa 24:15). Popanda kusankha, palibe kulambira kapena chikondi chenicheni.

Ahebri 3:15 amalimbikitsa kuti munthu ali ndi udindo wakusankha: “Lero ngati mudzamva mau ake, musaumitse mitima yanu.” Popeza tili ndi ufulu wosankha, timatha kumvera kapena kukana Mulungu. Paulo analemba kuti: “Kwa iye amene mudzipereka eni eni kukhala akapolo a kumvera... mukhalatu akapolo ake” (Aroma 6:16). Aliyense ali ndi udindo pa tsogolo la moyo wake. Petro akuchenjeza za: “kuchita changu kukhazikitsa maitanidwe ndi masankhulidwe anu” (2 Petro 1:10). Ngati panalibe ufulu wosankha, mapempho oterowo sangakhale ofunikira.

Kulandira kapena kukana chisomo

Zosankha za anthu kunja kwa chifuniro cha Mulungu sizimanyozera ulamuliro Wake koma zimaunetsera. Mwa lamulo Lake, ufulu wakudzisankhira ulipo, ndipo udindo wosankha uli pa moyo uliwonse. Mwa kulinganiza kwaufumu wa Mulungu, zili kwa munthu aliyense kulandira kapena kukana chisomo cha chipulumutso. Khristu waima

(Yapitirira pa tsamba 6)

pakhomo la mtima uliwonse nagogoda: “Ngati wina amva mau anga, nakatsegula chitseko, ndidzalowa kwa iye” (Chivumbulutso 3:20). Chipulumutso chiyenera kulandiridwa. Munthu aliyense ayenera kusankha: “Musalandire chisomo cha Mulungu kwachabe” (2 Akorinto 6:1).

Yesu anayang’ana Yerusalemu ndi chisoni: “Ine ndinafuna kangati kusunghanitsa pamodzi ana ako...koma inu simunafune ai” (Mateyu 23:37). Ambuye anafuna kukhala Mpulumutsi wao, koma anamkana Iye. Stefano anadzudzula atsogoleri achipembedzo, “Mukaniza



**“Kusankhidwa
kwa chisomo
kumagwirizanitsa
ulamuliro wa
Mulungu ndi
kuyankha kwa
munthu popeza iwo
amene akhulupirira
amasankhidwa,
osati
mokakamizidwa,
koma mwa chisomo.**

Mzimu Woyera nthawi zonse” (Machitidwe 7:51). Felikisi anali wotsimikiza mtima ndipo anakopeka kulapa, komabe anasankha kukana (Machitidwe 24:25). Yesu “pamene anakonzeka wamphumphu anakhala kwa onse akumvera iye chifukwa cha chipulumutso chosatha” (Ahebri 5:9). Mulungu amaitana munthu aliyense payekha, koma munthuyo payekha ayenera kuvomereza kapena kukana chipulumutso.

Kusankhidwa mwa chisomo

Ngakhale kuti chipulumutso chimaperekedwa kwa onse, ndipo munthu aliyense ayenera kusankha momwe angayankhire, Baibulo limanenanso za kusankha kwa Mulungu—kusankha kwake kopambana mwa chisomo. Talingalirani momwe kuiitana kwa Mulungu ndi mayankho a munthu zimagwirira ntchito limodzi mkati mwa cholinga Chake chamuyaya ndi kudziwiratu. Chipulumutso sichinali chongoganiziridwa pambuyo

pake—chinali chimene Mulungu mwaumulungu wake anaikiratu nthawi isanayambe. Dongosolo la chiombolo la Mulungu linali lokonzedweratu. Monga momwe Paulo analembera, Mulungu “anatipulumutsa ife, natiitana ife ndi maitanidwe oyera, si monga mwa ntchito zathu, komatu monga mwa chitsimikizo cha Iye yekha, ndi chisomo, chopatsika kwa ife mwa Khristu Yesu nthawi zisanayambere.” (2 Timoteo 1:9).” Dziko lisanalengedwe, Mulungu anakhazikitsa dongosolo la chisomo kudzera mwa Yesu Khristu. Ngakhale kuti anakhazikitsa mwadongosolo lake, anaphatikizapo njira imene anthu akanalandirira chipulumutso, kudzera mwa chikhulupiriro ndi kumvera.

Kukonzertu

Pa Aefeso 1:4-5 amati, “Anatisankha ife mwa Iye lisanakhazikike dziko lapansi...anatikonzertu tikalandire ngati ana a Iye yekha mwa Yesu Khristu.” Osankhidwa, ndi iwo omwe amabwera kwa Khristu mwa chikhulupiriro.

Vesi 11 likuonjezera kuti, “Mwa Iyenso tinayesedwa akeake olandira cholowa, popeza tinakonzekera mwa mwa chitsimikizo mtima cha Iye wakuchita zonse monga mwa uphungu wa chifuniro chake.” Mulungu anakonzertu dongosolo limene okhulupirira adzalandirira cholowa, osati mndandanda woikidwiratu wa anthu, koma cholinga chake chimene anawakonzertu onse omvera Khristu.

Chipulumutso sichinali cha gulu limodzi la anthu. Paulo anaphunzitsa m’zolembe zake zonse kuti dongosolo la Mulungu likuphatikizapo Ayuda ndi Amitundu. Aroma 8:28-30 amaphunzitsa kuti iwo amene Mulungu anawadziwiratu, Iye anawakonzertu. Kuitana kwa Uthenga Wabwino kunatsimikiziridwa Khristu asanabwere ndi kufalikira kwa onse. Njira ya chipulumutso ndiyokhazikika: “Pakuti palibe dzina lina pansa pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo” (Machitidwe 4:12). Mulungu sanasankhiretu amene adzakhulupirira, koma kuti amene akhulupirira adzapulumutsidwa.

Lemba la 2 Atesalonika 2:13 limati: “Mulungu anakusankhani inu kuyambira pachiyambi, mulandire chipulumutso mwa chiyeretso cha Mzimu ndi chikhulupiriro cha choonadi.” Kusankha kwa Mulungu sikusiyana ndi kuvomera kwaumunthu. Osankhidwawo ndi amene akhulupirira. Petro akutsimikizira zimenezi mu 1 Petro 1:2, pamene akuti oyera mtima anasankhidwa “monga mwa kudziwiratu kwa Mulungu Atate.” Chisankho cha Mulungu chopereka chipulumutso kwa onse okhulupirira, Ayuda ndi Amitundu omwe chimaulula chinsinsi cha kusankhidwa ndi kukonzedweratu. Sizitengerasno fuko kapena mtundu, ana a Mulungu tsopano asankhidwa mwa chisomo kudzera mu chikhulupiriro.

Chowonadi chimenechi chikutsimikizidwa pa Yohane 1:11-13: “Anadza kwa zake za iye yekha, ndipo ake a mwini yekha sanamlandire Iye. Koma onse amene anamlandira Iye, kwa iwo anapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu, akukhulupirira dzina lake; amene sanabadwe ndi mwazi kapena ndi chifuniro cha munthu, koma cha Mulungu.” Ngakhale kuti Ayuda monga mtundu anakana Khristu, onse amene anamlandira Iye anakhala ana a Mulungu, osati mwa chibadwa kapena chifuniro cha munthu, koma mwa chikhulupiriro mwa Khristu.

Kusankha ndi kwanu

Paulo anamaliza pa Aroma 11:5: “Choteronso nthawi yatsopano, chilipo chotsalira monga mwa kusankha kwa chisomo.” Kusankhidwa kwa chisomo kukutanthauza iwo amene akhulupirira molingana ndi dongosolo la Mulungu. Chisankho sichinangochitika mwachisawawa, koma dongosolo la chisomo cha Mulungu kwa onse amene avomera uthenga wabwino. Maitanidwewo ndi a anthu onse, koma amene akuvomera ndiwo osankhidwa.

Kusankhidwa kwa chisomo kumagwirizanitsa ulamuliro wa Mulungu ndi kuyankha kwa munthu popeza iwo amene akhulupirira amasankhidwa, osati mokakamizidwa, koma mwa chisomo. Dongosolo lakhazikitsidwa, nsembe yachitika, chipulumutso chaperekedwa ndipo tsopano, kusankha ndikwanu! ■



Ngati umunthu wa munthu uli woipitsidwa kotheratu, zingatheke bwanji kuti munthu asankhe kapena afunefune Mulungu?

Mneneri Yeremiya analongosola mkhalidwe wauchimo wa munthu kuti: “Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosachiritsika, ndani angathe kuudziwa? (Yeremiya 17:9). Paulo anatsindika mfundo imeneyi pa Aroma 3:10 “Palibe mmodzi wolungama, inde palibe mmodzi.” Vesi 12 likuwonjezera kuti: “Palibe mmodzi wakuchita zabwino.” Asanapulumeke, munthu aliyense ali mumkhalidwe woipa. Izi zizikutanthauza kuti anthu sangathe kuchita chilichonse choongoka, koma kuti palibe amene ali wolungama pamaso pa Mulungu, popeza onse akufunikira chipulumutso.

Mu Aroma 3, Paulo analankhula ndi Ayuda, kuwaonetsa kuti iwo sanali oposa Amitundu, chifukwa onse anali ofanana panso pa uchimo. Popanda chipulumutso, aliyense amalephera kufikira pa chiyero cha Mulungu. Mu vesi 11, Paulo anati: “Palibe mmodzi wakulondola Mulungu.”

Izi zikubweretsanso funso lakuti: Kodi wochimwa amene ali mumkhalidwe woipa angafunefune bwanji Mulungu? Yesu anayankha izi molunjika nati: “Kulibe mmodzi akhoza kudza kwa Ine koma ngati Atate wondituma Ine amkoka iye” (Yohane 6:44). Zimatengera kuti Mzimu amukoke ndi kubweretsa munthu wosabadwanso pamalo opangira chisankho. Palibe amene amafuna Mulungu popanda chisomo ichi. Koma uthenga wabwino ndi wakuti chisomo chokokachi chimafikira anthu onse.

Yesu ananena kuti Mzimu Woyera anatumizidwa “kudzatsutsa dziko lapansi za machimo, ndi za chilungamo,

ndi za chiweruzo” (Yohane 16:8). Iye ananenanso kuti: “Ndipo Ine, m’mene ndikakwezedwa kudziko, ndidzakoka anthu onse kwa Ine ndekha” (Yohane 12:32). Ananenanso kuti: Lemba la Yohane 1:9 limafotokoza kuti Yesu ndi “Uku ndiko kuunika kwenikweni, kumene kuunikira anthu onse akulowa m’dziko lapansi.” Chisomo chodzudzula ichi ndi chokoka sichili ku gulu lokonzedweratu koma chimafikira onse, ngakhale wochimwitsitsa koposa. Yesu anabwera “kufunafuna ndi kupulumutsa chotayikacho” (Luka 19:10).

Mulungu ndiye woyambitsa. Amaitana, amatsutsa, amawunikira, ndipo amakokera kwa Iye mwini. Komabe wochimwa ayenera kuyankha mwa chikhulupiriro kapena kukana chisomo ichi. Ngakhale kuti palibe amene amafunafuna Mulungu mwa iye yekha, aliyense amakokedwa, motero udindo woyankha uli pa moyo uliwonse. Ngakhale chikhumbo chaching’ono cha Mulungu sichichokera mwa ife tokha, uwu ndi umboni wa chisomo chake chotikokera kwa Iye.

Ngati Yesu anati, “Simunandisankha Ine, koma Ine ndinakusankhani inu,” kodi zikutanthauza kuti ife singathe kusankha pa za chipulumutso?

Ayi. Chipulumutso chimaperekedwa mwaulere, koma sichimakamizidwa kwa aliyense. “Iye amene afuna, atenge madzi a moyo kwaulere” (Chivumbulutso 22:17).

Lemba tikunenalo ndi Yohane 15:16: “Inu simunandisankhe Ine, koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi kubala chipatso.” Mau akuti ndinakusankhani apapa akuchokera ku muzu womwewo wa mau akuti sankha. Pophunzira Mau a Mulungu, chofunika kwambiri ndi chakuti nkhanayo ikukamba chiyani.

Mu ndime iyi, Yesu analankhula makamaka kwa ophunzira ake. Khristu ndi amene anawaitana ndi kuwadzoza kuti apite kukalalikira uthenga wabwino. Maitanidwe awo ndi mphatso zauzimu sizinali zochokera kwa iwo okha koma zinali zochokera kwa Mulungu. Ngakhale pali maitanidwe a anthu onse a chipulumutso, ndime iyi ikunena za kuitanira kwa ophunzira ku utumiki ndi kutumikira, koma osati munthu sangathe kusankha pa za chipulumutso.



Kodi Aroma 9 amaphunzitsa kuti Mulungu amasankha amene adzapulumuke ndi amene adzataike?

Ayi. Aroma 9 akutsindika kuti Mulungu ali ndi mphamvu yodalitsa aliyense amene Iye wafuna ndi kukwaniritsa cholinga chake cha chiombolo. Siiphunzitsa kuti chipulumutso chimangochitika mwachisawawa. Pamene Mulungu ananena kuti, “Ndinakonda Yakobo, koma ndinamuda Esau” (v.13), sanali kunena za Yakobo ndi Esau monga munthu aliyense payekha, koma zidzukululu zao. Iye anali kunena za mitundu ndi maudindo awo m’chifuniro chake, osati chipulumutso cha munthu aliyense payekha. Iye pokhala Mulungu, muulamuliro wake, anasankha kudalitsa zidzukululu za Yakobo pamwamba pa mitundu yonse, kotero ali ndi ulamuliro ndi ufulu wotsegulira dongosolo la chipulumutso kwa Amitundu. Osankhidwawo sakusankhidwanso popeza anabadwa kwa Ayuda, koma kubadwa mwauzimu.

“Ndidzachitira chifundo amene ndimchitira chifundo” (v.15) akufotokoza kuti Mulungu ali okonzeka kupereka chifundo. Komabe malemba ena amasonyeza kuti Iye amapereka chifundo ndi chipulumutso kwa anthu onse. Pamene Paulo akulemba kuti, “Sichifuma kwa munthu amene afuna...” (v.16), akutsindika kuti chipulumutso sichimapezeka mwa mphamvu ya munthu koma mwachisomo. Aroma 9 amatsimikizira kuti Mulungu ali ndi ufulu wochitira chifundo pa zimene Iye amafuna, komabe mauwo akuitanirabe onse kuti avomere mwachikhulupiriro.

Ndimeyi ilinso ndi chenjezo: pamene wina apitiriza kukana zochita za Mulungu, ndipo Mulungu achotsa kukhudzika kwa Mzimu Wake, mtima wa munthuyo umauma.



KODI MUKUDZIWA?

Ziphunzitsa za Calvinism ndi Arminianism zimaimira malingaliro awiri akuluakulu a zaumulungu pa chipulumutso. Calvinism imazikika pa ziphunzitsa za John Calvin (1509-1564), ndipo chimatsindika pakuti Mulungu ali ndi ulamuliro pa china chilichonse, kuphatikizapo kukonzedweratu, ndipo chimakhulupirira kuti Mulungu amasankha anthu kuti akhale ndi moyo wosatha. Arminianism imazikika pa malingaliro a Jacob Arminius (1560-1609), ndipo imatsindika pa ufulu wa munthu wodzisankhira, kunena kuti anthu akhoza kuvomereza kapena kukana chisomo cha Mulungu. Malingaliro awiriwa amasiyana pa kusankha, chisomo, ndi kulimbikira ndipo pakhala pali mtsutso kwa zaka mazana ochuluka.

Ndi dalitso lotani nanga kuimirira pa kuitana kophweka, komveka bwino kwa Khristu kwakuti: “Idzani kuno kwa Ine... ndipo Ine ndidzakupumulitsani inu” (Mateyu 11:28).



**Mau a
Nyengo
Yake**

PITIRIZANI KUITANA— MULUNGU AKUITANABE

Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org

Tuluka, nupite kumiseu ndi njira za kuminda, nuwaumirize anthu alowe, kuti nyumba yanga idzale. — Luka 14:23

Zitha kukhala zofooketsa kugawana uthenga wabwino ndi ena koma kukumana ndi kukanidwa, kusolidwa, kapena kusalandiridwa. Yesu anakumana nazo zimenezi, ndipo ifenso tidzatero. Komabe, Mulungu akuitanabe, ndipo kuitanako sikunathe. Khomo la chisomo likadali lotseguka. Udindo wathu suli kusankha amene angayankhe koma kulengeza mokhulupirika za kuitanako.

Ngakhale mu utumiki wa Paulo, ena ananyodola, ena anachedwa, ndipo ena anakhulupirira. Zotsatirazo zinali zosiyana, koma kuitana kunakhalabe kosasintha. Pitirizani kulalikira. Pitirizani kukonda. Pitirizani kutumikira. Pitirizani kuitana.



Pali mitima yomwe imati “inde”. Palinso ana olowerera amene adzabwerera. Pali miyoyo yomwe ili ndi njala ya choonadi, yolakalaka chiyembekezo, ndi yokonzeka kulandira mwinjiro wa chilungamo. Iwo sangabwere mwaunyini, koma ngakhale wochimwa mmodzi wopulumutsidwa amabweretsa chisangalalo chachikulu Kumwamba. Mbeu zimene timafesa sizibala zipatso nthawi yomweyo, ndipo zotsatira zake si udindo wathu. Maitanidwe athu ndi kungofesa mbeu yabwino ya uthenga wabwino.

Anthu akamavomera, sizikhala chifukwa cha kulankhula kwathu, luso lathu, kapena nzeru zathu, zidzakhala mwa chifundo ndi chisomo cha Mulungu. Zimenezi ziyenera kutipatsa mphamvu yoitana mopanda mantha. Sitiyenera kuzengereza kuuza anthu za Yesu, popeza sitikupereka chinthu chofooka kapena chosatsimikizika. Timalengeza mphatso yaikulu kwambiri padziko lapansi, imene ili chipulumutso.

Popeza nthawi ya chiweruzo ikanalipo, ntchito siinathe. Na ngati pali moyo, Mulungu akuitanabe. Pokhala Iye akuitanabe, nafenso tiyenerabe kuitana. Tiyeni tifulumizidwe kupita ku misewu ndi mipanda ndikukakamiza anthu kuti abwere. Pali anthu miyandamiyanda amene akusowa machiritso, chisomo chopulumutsa cha Yesu Khristu. Koteri, ife tiyeni tipite ndi kukalalikira uthenga wina umodzi, kupempherabe pemphero lina limodzi, kufikira moyo winanso umodzi.

Munthu akapulumutsidwa, ulemmero wonse umapita kwa Mulungu. Koma zimadzetsa chisangalalo chozama kukhala kagawo kakang’ono ka ntchito yaikulu yaumulungu imeneyi. Iwe wantchito mnzanga wa uthenga wabwino, pitiriza kuitana, pakuti Mulungu akuitanabe. ■

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

